

CHITHUNZI CHA CHIKONDI



Phunziro 7, August 15, 2026

“Ndipo tsopano zatsala zinthu zitatu: chikhulupiriro, chiyembekezo ndi chikondi. Koma chachikulu pa zonsezi ndi chikondi” (1 Akorinto 13:13, CCL)



1 Akorinto 13 imadziwika kuti ‘mutu wa chikondi.’ Sikunena za chikondi cha pakati pa anthu okondana, koma chikondi chozama kwambiri: chikondi cha Mulungu.

Paulo akufotokoza bwino kwambiri mmene tingasonyezere m’miyoyo yathu chikondi cha Mulungu chimene chatsanulidwa m’mitima mwathu (Aroma 5:5).

Chikondi ndi chimene chimatilimbikitsa pa zochita zathu zonse, ndipo ndi chifukwa chake timachita zinthu zimene zimapindulitsa anthu amene timachita nawo zinthu.



CHITHUNZI CHA CHIKONDI

**Kupambana kwa
chikondi**

Makhalidwe a chikondi

**Kupirira kwa
chikondi**

**Njira
yopambana
koposa**

**Zimene
chikondi
chimachita**

**Zimene
chikondi
sichima-
chita**

**Chithinzi
cha Yesu**

**Makhalidwe
opambana**

KUPAMBANA
KWA
CHIKONDI



NJIRA YOPAMBANA KOPOSA

“Koma funitsitsani mphatso zopambana. Tsopano ndikuonetsani njira yopambana kwambiri.” (1 Akorinto 12:31 cCL)



Kodi Paulo akufotokoza chikondi chotani mu 1 Akorinto 13, ndipo ndichifukwa chiyani chikondi chimenechi chimaposa mphatso iliyonse ya uzimu? (1 Akorinto 12:31–13:3)

MuChigiriki muli mawu angapo ofotokoza chikondi. Paulo akusankha mawu akuti agape (chikondi chosadzikonda, chopanda malire, chimene chimaganizira ena ndipo chimangofunafuna ubwino wa wokondedwayo). Ndi mawu omwewo amene Yohane amagwiritsa ponena kuti ‘Mulungu ndiye chikondi’ (1 Yohane 4:8).



Palibe mphatso ya Mzimu imene imakhala yothandiza ngati siigwiritsidwa ntchito motsogozedwa ndi chikondi choterechi. Ndipotu, zochita ndi maganizo athu onse ziyenera kudzazidwa ndi chikondi cha agape.



Yesu anatichenjeza kuti, chifukwa cha kuchuluka kwa zoipa, chikondi chimenechi chidzazirala (Mateyu 24:12). Koma tisalole kuti zimenezi zichitike kwa ife, m’mabanja mwathu, kapena m’mipingo mwathu.



MAKHALIDWE A CHIKONDI



ZOMWE CHIKONDI CHIMACHITA

**Ndicholeza
Mtima**

makrothymeō: Kukhala woleza mtima, kupirira, ndi kukhala wopirira kwa nthawi yaitali

Kukhala woleza mtima ndi kupirira zolakwa za ena

**Ndichokoma
mtima**

jrēsteuomai: Kuchitira ena zabwino

Ndichachifundo ndipo chimamvera ena chisoni

**Chimakondwera
ndi choonadi**

synjairō: Kusonyeza chifundo ndi kukondwera limodzi ndi ena

Chimakondwera limodzi ndi amene amachirikiza choonadi

**Chimatchinjiriza
nthawi zonse**

stegō: Kusalankhula za zolakwa za ena (koma kuzipirira moleza mtima)

Chimabisa zolakwa za ena ndi kukhala chete osaziulula

**Chimakhulupirika
nthawi zonse**

pisteuō: Kukhala ndi chikhulupiriro, kukhulupirira, ndi kudalira

Sichifulumira kuweruza ena, koma chimawapatsa mwayi poganiza kuti mwina sanalakwitse

**Chiyembekezo
nthawi zonse**

Elpizō: Kuyembekezera kapena kudalira

Nthawi zonse chimayembekezera kuti zinthu zabwino zichitike

**Chimapirira
nthawi zonse**

hypomenō: Kupirira, kulimbana ndi zovuta, kukhala wolimba mtima, ndi kupitirizabe osafooka

Chimapirira mavuto, mayesero, ndi mazunzo

“Chikondi n’choleza mtima, chikondi n’chokoma mtima; [...] chimakondwera ndi choonadi; Chimatchinjiriza nthawi zonse, chimakhulupirika nthawi zonse, chimakhala ndi chiyembekezo nthawi zonse, chimapirira nthawi zonse.” (1 Akorinto 13:4-7 CCL)



ZOMWE CHIKONDI SICHIMACHITA

"[...] chilibe nsanje, sichidzikuza, sichidzitamandira. Chikondi chilibe mwano, sichodzikonda, sichipsa mtima msanga, sichisunga mangawa. Chikondi sichikondwera ndi zoyipa[...]" (1 Akorinto 13:4-7 CCL)



Chilibe nsanje

zeloō: Kukhala ndi mtima woyaka

Sichichita nsanje ndi omwe ali ndi mphatso kapena makhalidwe ena abwino

Sichidzikuza

perpereuomai: Kudzitamandira kapena kudzikweza

Sichifuna kutamandidwa ndi ena

Sichidzitamandira

fysioō: Kudzikuza kapena kukhala wonyada

Sichidziona kukhala opambana kuposa m'mene mwini aliri

Chilibe mwano

asjēmoneō: Kuchita zinthu mosayenera

Sichichita zinthu zosemphana ndi makhalidwe abwino ndiponso miyambo yoyenera ya anthu

Sichodzikonda

zēteō: Kufufuza

Chimalolera kusiya ufulu wake kuti ena apindule

Sichipsa mtima msanga

paroxynō: Kukwiyaitsa, kuputa, kapena kuchititsa munthu kukwiya kwambiri

Sichifulumira kukwiya, ndiponso sichikhumudwa mosavuta

Sichisunga mangawa

logizomai: Kusunga chiwerengero cha zolakwa

Chimakhululuka ndipo sichisunga mumtima zolakwa zimene ena achita

Sichikondwera ndi zoyipa

jairō: Kukhala wokondwa, kusangalala, kapena kumva bwino

Sichikondwera ndi zolakwa za ena, koma chimayesetsa kuwathandiza kuti akonze zolakwazo

CHITHUNZI CHA YESU

"Lamulo langa ndi ili: 'Kondanani wina ndi mnzake monga Ine ndakonda inu.'" (Yohane 15:12 CCL)

Anapirira
kumenyedwa,
kunyozedwa, ndi
kuchitidwa
chipongwe
(Mateyu 27:27-31)

Ndioleza
Mtima



Ankasamala za
aliyense amene
anali kuvutika

Ndiokoma
mtima



Ankaphunzitsa
choonadi
momveka bwino
komanso
motsimikiza

Amakondwera
ndi choonadi



Iye sanaweruze
mkazi wochimwayo
koma
anamukhululukira
(Yohane 8:10-11)

Amatchinjiriza
nthawi zonse



Anakhulupirira
kuti kulapa kwa
Zakeyu kunali
koona
(Luka 19:8-9)

Amakhulupirika
nthawi zonse



Anakonzekeretsa
amuna 12 kuti
agwire ntchito
imene inkaoneka
ngati 'yosatheka'

Ali ndi
chiyembekezo
nthawi zonse



Anapirira njala,
kukanidwa,
zowawa, ndi
masautso

Amapirira
nthawi zonse



CHITHUNZI CHA YESU

"Lamulo langa ndi ili: 'Kondanani wina ndi mnzake monga Ine ndakonda inu.'" (Yohane 15:12 CCL)

**Sanafune ulemu,
ndipo ankacheza
ndi anthu
odzichepetsa**

**Sachita
nsanje**



**Ngakhale kuti anali
Mfumu ya
Chilengedwe Chonse,
sanadzitamandire
chifukwa cha
zimenezo**

**Sadzionetsera
yekha**



**Anali wokonzeka
kugwira ngakhale
ntchito zonyozeka
kwambiri**

Sadzikuza



**Ankachitira
aliyense zinthu
mwaulemu ndi
moyenera**

**Sachita zinthu
mwamwano**



**Ankachita
chifuniro cha
Atate wake nthawi
zonse (Yohane
6:38)**

**Sasamala
zake zokha**



**Ngakhale pamene
anamumenya,
anayankha
mwaulemu
(Yohane 18:22-23)**

**Sakwiya
msanga**



**Anapempha kuti
amene
anamupachika
akhululukidwe
(Luka 23:34)**

**Saganiza
zoyipa**



**Analankhula
mwamphamvu
kwa Afarisi
osalungama
(Mateyu 23:27-28)**

**Sakondwera
ndi
zosalungama**



KUPIRIRA KWA CHIKONDI




MAKHALIDWE OPAMBANA

"Ndipo tsopano zatsala zinthu zitatu: chikhulupiriro, chiyembekezo ndi chikondi. Koma chachikulu pa zonsezi ndi chikondi." (1 Akorinto 13:13 CCL)

Akorinto, mwa khalidwe lawo, anali kusonyeza zinthu zimene chikondi sichichita: anali ansanje; odzitamandira; odzikuza; ankachita zinthu mosayenera; anali odzikonda; ankakwiya msanga; anali ndi mtima wosunga zakukhosi; ndipo ankalekerera tchimo

Monga iwo, ifenso tiyenera kusiya makhalidwe oipawa ndi kukhala ndi makhalidwe a chikondi mochuluka, monga Paulo akutiphunzitsira, kuti tigwiritse ntchito mphatso za Mzimu moyenera. Akutilimbikitsanso kuti tikhalebe ndi makhalidwe ena awiri: chikhulupiriro ndi chiyembekezo.



Yesu akadzabwera, tchimo lidzatha, ndipo tidzasangalala ndi moyo wosatha limodzi ndi lye. Pamenepo, uneneri, malilime, ndi mphatso zina, kuphatikizirapo chikhulupiriro ndi chiyembekezo, sizidzafunikanso. Koma chikondi chidzakhalapo mpaka muyaya (1 Akorinto 13:8).

“Mulungu ndiye chikondi. Chikondi cha Atate ndi cha Mwana ndi khalidwe limene liyenera kuoneka mwa wokhulupirira aliyense. Mawu a Mulungu ndi njira imene chikondi cha Mulungu chimafikira kwa munthu. Choonadi cha Mulungu ndi njira imene imafikira maganizo a munthu. Mzimu Woyera amaperekedwa kwa munthu amene amagwira ntchito mogwirizana ndi mphamvu za kumwamba. Iye amasinthira maganizo ndi khalidwe la munthu, ndikumuthandiza kupirira ngati akuona Iye amene saoneka. Chikondi changwiro tingakhale nacho ngati tikhulupirira choonadi ndi kulandira Mzimu Woyera.”

EGW (Our Father Cares, October 9)